Mmene Zochita za Angelo Komanso Ziwanda Zimakhudzira Moyo Wathu (Gawo 2)

Nkhaniyi yachokera m'mutu 10 wa buku lakuti, *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* lomwe likupezeka pa jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso zifukwa zake. Fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, kenako ganizirani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.



KODI KUKHULUPIRIRA MIZIMU N'KULAKWA?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

N'chifukwa chiyani anthu ena angayankhe kuti ayi?

N'chifukwa chiyani anthu ena angayankhe kuti inde?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

Nanga n'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Baibulo limaletsa kuti tizichita zinthu zokhudza kukhulupirira mizimu, zomwe ziwanda zimagwiritsa ntchito posocheretsa anthu.
(Werengani mutu 10 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 9 mpaka 13.)

Werengani Deuteronomo 18:10, 11 ndi Agalatiya 5:19-21.
Kodi malembawa akusonyeza kuti Yehova amaiona bwanji nkhani ya kukhulupirira mizimu?

Werengani Chivumbulutso 12:12, 17.
N'chifukwa chiyani Satana ndi ziwanda zake amayesetsa kusocheretsa anthu?

Ngati simungalole kuti chigawenga chilowe m'nyumba mwanu, kodi mungachite zinthu zomwe zingaitane ziwanda kuti zizisokoneza moyo wanu?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Yehova angatithandize kuti tithe kulimbana ndi ziwanda.

(Werengani mutu 10 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 14 mpaka 19.)

Werengani Machitidwe 19:19.

Kodi lembali likusonyeza bwanji kuti Akhristu a ku Efeso anali chitsanzo chabwino pokana kukhulupirira mizimu?

Werengani Miyambo 18:10; Aefeso 6:16 ndi Yakobo 4:7, 8.

Kodi Yehova watipatsa zinthu ziti zimene zimatithandiza kulimbana ndi Satana ndi ziwanda zake?

Kodi mfundo yakuti Yehova ndi wamphamvu kuposa ziwanda ndiponso kuti amafunitsitsa kutithandiza ingatilimbikitse bwanji?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI…

Palibe vuto lililonse ngati munthu akulosera za m’tsogolo.

MUNGANENE KUTI…

Anthu ambiri akhoza kuganiza choncho. Koma ine ndimakhulupirira zosiyana ndi zimenezo chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze zotani kuti munthuyo amvetse bwino lembalo?

_____

WINA AKANENA KUTI…

Ziwanda ndi zamphamvu kwambiri ndiye sitingathe kulimbana nazo.

MUNGANENE KUTI…

N’zoona kuti ziwanda ndi zamphamvu. Koma ndimakhulupirira kuti *tikhoza* kulimbana nazo chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze zotani kuti munthuyo amvetse bwino lembalo?

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania